



M'busa Tony Alamo chithunzi—1992

KUPUMULA MU NTHAWI YA MAVUTO

Yolembedwa ndi Tony Alamo

“Ndipo kwa inu amene mukusautsidwa mudzapeza mpumulo pamodzi nafe” (2 Atesalonika 1:7). Pamene tasautsidwa, Ambuye akutilamula ife kuti tipumule mwa Iye. Inde! Tikuyenera kupuma kape-na kusunga Sabata mwa Iye. Pumulani mu Mawu (Yohane 1:14).

Yesu akuti, “Idzani kwa Ine, nonsenu akulema ndi akuthodwa, ndipo ndidzakupumultsani inu. Senzani goli Langa [ntchito], ndipo phunzirani kwa ine; chifukwa ndine wofatsa ndi wodzichepetsa mu mtima: ndipo mudzapeza mpumulo wa miyoyo yanu. Pakuti goli Langa [ntchito] liri lofewa, ndipo katundu Wanga ali wopepuka” (Mateyu 11:28-30). Yesu akufuna ife tiphunzire Mawu Ake, amene ali Iye, ndikuchita zimene Iye akunena, chifukwa tikachita zimene akunena, tidzaona kuti Mawu Ake ndi utsogoleri Wake ndi zoona kumiyoyo yathu.¹ Mwa njira iyi, chikhulupiliro chathu chidzakula (Aroma 10:17).

Yesu amene anakhala munthu anali womvera pamaso pa Mulungu Atate; Iye anachita ndi kuchita chili chonse chimene Atate amamuza kuti achite, zimene zili tanthauzo la kumvera.² Iye anapumulira mwa Atate ndipo anali wodekha mum-

tima: Sanadzitukumule pamaso pa Atate. Yesu ndi osiyana kwambiri ndi Satana, amene ali odzadza ndi matukutuku, ndikudzitamandira kuposa Mulungu.³ Ndipo ndi woipa kwenikweni!

Mu 2 Atesalonika 1:7-12, Paulo anati tikhonza kupumula mwa anthu a Mulungu mu ola lino la vuto la lero pamene mdierekezi akuononga mizinda ya dziko ndikupanga dziko kukhala chipululu.⁴ Iye anati, “Pa nthawi imene Ambuye Yesu adzaonekere kuchokera Kumwamba limodzi ndi angelo Ake amphamvu, m'moto walawilawi kubwenzera chilango kwa iwo onse osam'dziwa Mulungu, ndi kwa anthu osamvera uthenga wabwino wa Ambuye wathu Yesu Khristu: Amene adzalangidwe ndi chiwonongeko chamuyaya kuchoka pamaso pa Ambuye, ndi kuchoka ku ulemerero wa mphamvu Zake; Pamene Iye adzadza kudzalemekezedwa mwa oyera mtima Ake, ndi kukhala wodabwitsa mwa onse akukhulupilira (popeza munakhulupilira umboni wathu wa kwa inu) m'tsiku lija. Kukatero tikupemphereraninso nthawi zonse, kuti Mulungu wathu akakuyeseni inu oyenera kuitanidwa kwanu, nakakwaniritsa chomkomera Iye chonse, ndi

ntchito ya chikhulupiliro mu mphamvu: Kuti dzina la Ambuye wathu Yesu Khristu lilemekezedwe mwa inu, ndi inu mwa Iye, monga mwa chisomo cha Mulungu wathu, ndi kwa Ambuye Yesu Khristu.”

Tsopano tikukhala mu nthawi imene inaloseledwa mu Danieli 12:1: “Ndipo nthawi yomweyi adzauka Mikaeli, kalonga wamkulu wakutumikira ana a anthu a mtundu wako: ndipo padzakhala nthawi ya masautso, imene siinakhalepo chiyambireni mtundu wa anthu kufikira nthawi yomwe ija: ndipo nthawi yomweyo anthu ako adzapulumutsidwa [Mulungu adzapulumutsa ife amene tili ndi chikhulupiliro cha ku-pumula mwa Iye], yense amene ampeza wolembedwa m'bukhu [Bukhu la Moyo]. Ndipo ambiri a iwo ogoni mu fumbi la dziko lapansi adzauka, ena kunka ku moyo wosatha, ndipo ena ku manyazi ndi mnyozo wosatha. Ndipo iwo akuzindikira adzawala ngati kunyezimira kwa thambo; ndi iwo amene akuthandiza anthu ambiri kukhala olungama adzawala ngati nyenyezi mpaka kalekale. Koma iwe, O Danieli, sunga mawu awa, ndipo utseke ndi kumata bukhu, ngakhale mpaka nthawi ya chimaliziro:

(Yapitirira patsamba 2)

KUPUMULA MU NTHAWI YA MAVUTO

(Yachokera patsamba 1)

ambiri adzathamangira uku ndi uku, ndipo adzadziwa zinthu zambiri zoona [Zinthu izi zimathandiza kuonetsa kuti tili m'amasiku otsiriza, mapeto a nthawi].

“Pamenepo ine Danieli ndinapenya, ndipo, taonani, anaimapo awiri ena, wina anaimirira m'mpheapete mwa mtsinje tsidya lino, ndipo wina anaimirira m'mpheapete mwa mtsinje tsidya linalo. Ndipo mmodzi anafunsa munthu wovala nsalu ya bafuta, amene anali pamwamba pa madzi a mumtsinje, Kodi zidzatenga nthawi yaitali bwanji kuti zinthu zodabwitsazi zithe? Ndipo ndinamva mwamuna wovala nsalu ya bafuta uja, amene anali pamwamba pa madzi a mumtsinje, pamene anakwenza dzanja lake lamanja ndi lamanzere Kumwamba, nalumbira pa Iye wokhala ndi moyo wosatha kuti zidzachitika kwa nthawi, ndi nthawi zina, ndi nusu; ndipo atatha kum-

waza mphamvu ya anthu opatulikawo zinthu zonsezi zidzatha” (Danieli 12:1-7).

Anthu oyera mtima akumwazika tsopano. “Anthu ambiri adzadzitsuka, ndi kudziyeretsa, nadzayesedwa [Osafooka; pumulirani mwa Ambuye!]; koma woipa adzachitazinthu zoipa: ndipo palibe munthu woipa aliyense amene adzamvetsetse mawu amenewa; koma anthu ozindikira adzawamvetsetsa” (Danieli 12:10).

“Mwa amene Mulungu wa nthawi ino ya pansi pano [mulungu wa dziko lino ndi mdierekezi] wachititsa khungu maganizo awo a osakhulupilira, kuti chiwalitsiro cha uthenga wabwino wa ulemelero wa Khristu, amene ali [onetsa] chithunzithunzi cha Mulungu, chisawawalire. Pakuti sitikulalikirira za ifeyo, koma za Khristu Yesu Ambuye; ndipo ifeyo akapolo anu chifukwa cha Yesu. Pakuti Mulungu amene analamula kuwala kuti kuunike kuchokera mu mdiima, ndiye amene anawala m'mitima yathu, kutipatsa chiwalitsiro cha chidziwitso cha ulemelero wa Mulungu pa nkhope pa Yesu Khristu. Koma tili nacho chuma ichi m'zonyamulira zoubidwa ndi dothi, kuti

ukulu woposa wamphamvu uchokere kwa Mulungu, osati kwa ife.

“Ndife osautsika mwamtundu uliwonse, koma osapsinjika; ndife osinkhasinkha, koma osakhala kakasi; ozunzidwa, koma osatayika; ogwetsedwa pansu, koma osonongeka; Nthawi zonse kukhala mu thupi kufa kwake kwa Ambuye Yesu, kuti moyonso wa Yesu uoneke m'thupi mwathu. Pakuti ife amene tili ndi moyo tiperekeka kuimfa nthawi zonse chifukwa cha Yesu, kuti moyonso wa Yesu uonekere m'thupi lathu lokhoza kufali.

“Choncho imfa ichita mwa ife, koma moyo kwa inuyo. Koma pokhala nawo Mzimu womwewo wa chikhulupiriro, monga mwa cholembedwacho, ndinakhulupira, chifukwa chake ndinalankhula; ifenso tili ndi chikhulupiriro, koterotikulankhula; Podziwa kuti Iye amene anaukitsa Ambuye Yesu adzaukitsanso ife pamodzi ndi Yesu, nadzatiikapo pamodzi ndi inuyo. Pakuti zonsezi zachitika chifukwa cha inu, kuti kukoma mtima kwakukulu kudzera m'mayamiko a anthu ambiri ku-

(Yapitirira patsamba 4)

India

Okondedwa M'bale,

Moni woyera kwa inu, M'busa wanga wa chikondi Tony Alamo, anzanu, okufunirani zabwino, abale a utumiki wanu wa Alamo, Tchalitchi chanu ndi ena onse mudzina la mtengo wapamwamba la Ambuye ndi Mpulumutsi wathu Yesu Khristu.

M'bale, ndalandira zolemba zanu zodabwitsa ndi ma Baibulo. Zikomo kwambiri chifukwa cha zolemba zanu ndi ma Baibulo anu ku ntchito yanga ya uzimu. Ambuye wathu watilumikiza kuti tilalike uthenga wa choonadi kumalo osiyanasiyana. Kamba ka ichi tikhonza kukhala okondwa. Chonde tikupereka mafuno abwino kwa inu, utumiki wanu wodalitsika wa Tony Alamo Ministry ndiponso makamaka M'busa Tony Alamo.

M'bale, ndine okondwa kwambiri kukudziwitsani kuti titalandira zolemba zanu zodabwitsa tinakhazikitsa kampeni ya Uzimu yofikira maderena otchedwa Rampachodavaram. Gulu lathu la uzimu pamodzi ndi ine mwa chisomo tinayenda khomo ndi khomo ku dera lonse ndi kugawa zolemba

zanu za uzimu kuti adziwe zolinga za Mulungu pa zachipulumutso. Usiku timapanga misonkhano ya uzimu ndikulungosola za mphamvu ya Mulungu ndi ufumu Wake. Ambiri analandira Khristu kukhala Mpulumutsi wawo ndipo anamva za uzimu wa Khristu mwa chidwi. Msonkhano wathu unachitika ndi cholinga cholemekeza Ambuye wathu. Kutumiza zithunzi za misonkhano ndi za ana amasiye kuti muthe kuona mwa chifundo chanu.

M'bale, chonde tumizirani mpingo wanga ma Baibulo oyera a chilankhulo cha Telugu. Chonde atumizireni anzanga ogwira nawo ntchito ndi amasiye zovala zovalidwa kale.

Chonde ndipemphererani, banja langa, ogwira nawo ntchito, amasiye, azimayi amene

amuna awo anamwalira, mipingo ndi ntchito yathu ya uzimu. Kuno tonse tikukupemphererani, umoyo wa M'busa wachikondi Tony ndi utumiki wanu wa Tony Alamo.

Tikudikilira yankho lanu labwino. Ambuye akudalitseni ndi onse. M'bale wanu mwa Ambuye M'busa A. David West Godavari District, Andhra Pradesh, South India



M'bale Rajaji Sadhanala ndi mamembala ena a mpingo kugawa uthenga wabwino wa M'busa Tony Alamo m'midzi ya Andhra Pradesh, India

Utumiki wa Alamo pa intaneti



M'busa Jonathan Brooks ndi M'bale Richard kugawa zolemba za Uthenga wabwino wa M'busa Alamo mumsika wa Monrovia, Liberia

Liberia

Moni M'busa Tony,

Ndidzakhala okondwa ndi zolemba zanu komanso ma T-shirt. Nthawi zonse tidzakhala nanu m'mapemphero.

Chomwe tikufuna ndi chakuti Utumiki uwu (Tony Alamo Christian Ministries) ukhale ndi nthambi kuno ku Africa, Liberia. Tikudziwa ndi kukhulupilira zidzachitika, chifukwa utumiki wanu ukusintha miyoyo ya anthu. Tikuyesetsa kumakumana ndi kuchita mapemphero pamodzi.

Anthu ambiri akusangalatsidwa ndi kuwerenga zolemba zanu, tiyeni tigwire ntchito limodzi ya Ambuye kuti tikope miyoyo yambiri.

Pemphero lathu ndi kugawa zolemba zanu kuno konse ku Liberia. Ndibwino kuphunzitsa wina choonadi. Zolemba za uthenga wanu wabwino zikuthandiza anthu padziko lonse kudziwa choonadi.

Anthu aku Liberia ndi maiko oyandikana nawo akufuna kuwerenga zolemba zanu za uthenga wabwino. Tikupemphera ndi kudikirira katundu kuti abwere mwa mphamvu ya Mulungu.

Jonathan Brooks

Monrovia, Liberia, Africa

Italy

Okondeka M'busa Tony Alamo,

Ndikuthokoza Mulungu chifukwa cha moyo ndi utumiki wanu. Ndili osangalala kukupatsani moni m'dzina la Ambuye wathu Yesu Khristu, ndi banja lanu, komanso mpingo wanu wonse mwa Ambuye. M'busa Tony, ndiliba zambiri zonena, koma kwanga ndi kukuthokozani chifukwa cha mphatso za mtengo wapatali—zolemba zanu ndi Baibulo. Ndima-konda kuziwerenga, pakuti zipatsa moyo.

Cholinga changa chenicheni cholembela kalatayi ndi kukuthokozani chifukwa

cha katundu wabwino kwambiri amene munanditumizira. Ndi mphatso ya mtengo wapatali kulandira m'nthawi ya masautso. Abusa, mukudziwa kodi? Ndinalandira katundu madzulo, pamene ndinali m'tsiku langa lachisanu ndili kusala kudya ndi kupemphera. Tangoganizani—anandiponyera kuwala kodabwitsa mu mzimu wanga, ndikuonjezera chikhulupiliro changa, ndipo ndikudziwa kuti ndi Mulungu zonse n'zotheka. Ndikhulupilira ndisanamalize kuwerenga zolembedwa zonse mwa phatikiza, moyo wanga sukhalanso chimodzimidzi.

Ndikufunanso kukudziwitsani kuti ndine gawo la utumiki wanu wodabwitsa. Chonde ndiphatikizeni ku mpingo wanu. Ndikupempha pemphero lanu ndi thandizo lili lonse loyenelera londithandiza kukhala munthu wa Mulungu, odzadzidwa ndi Mzimu, ndi kulalikirira choonadi cha uthenga wabwino, chifukwa ndi choonadi chokha chimene chimamasula munthu (John 8:32).

Ndatha ine wanu mokhulupirika,

Bismarck K. Sakyi

Ghedi, Italy

Thailand

Okondeka Abusa,

Moni wopatulika kwa inu, wodalitsika, ndipo mupitilize kupulumutsa miyoyo yambiri chifukwa cha ntchito ya Ambuye Wamphamvu zonse.

Zikomo kwambiri chifukwa choyankha kalata yathu yomalizira. Tina-landira phukusi limene munali zolemba ndi bukhu la Mesiya komanso makalata a nkhani. Tawerenga makalata a nkhani onse, ndipo anthu ambiri akupereka maumboni a zolemba zanu. Mu kalata yanu yobwera kwa

ife, munatiuza kuti tifunse za zolemba zanu zochulukana, ngati tikuzifuna, kotero chonde yesetsani kutithandiza kulandira zinanso, chifukwa zinthu ngati izi zimatithandiza.

Tikusala chakudya ndi kupemphera, ndipo enafe talandira mphamvu zamachiritso kuti tizichiza matenda a anthu kuno. Ngakhalsenso ine, ndikupeza bwino kwambiri, ndipo ndachiritsidwa. Zinthu zina zabwino zambiri zikuchitika, anthu akuona masomphenya ndiponso maloto.

Tikufuna chithandizo chonse m'mapemphero. Chikhulupiliro chimasuntha phiri. Zikomo, ndi zonse zathu zabwino. M'bale wanu mwa Khristu, Djiande Alexander Chatujack, Bangkok, Thailand



MAUTUMIKI A ALAMO PA INTANET

www.alamoministries.com

KUPUMULA MU NTHAWI YA MAVUTO

(Yachokera patsamba 2)

chulukitse mayamiko ku ulemelero wa Mulungu. Chifukwa chake sitikubwerera m'mbuyo; koma ngakhale umunthu wathu wakunja ukutha, komabe umunthu wathu wamkati ukonzedwanso mwatsopano tsiku ndi tsiku. Pakuti chisautso chathu chopepuka, cha kanthawi, chitichitira ife kulemera koposa kwakukulu ndi kosatha kwa ulemelero; pamene sitikuika maso athu pa zinthu zooneka, koma zinthu zosaoneka: pakuti zinthu zooneka n'zakanthawi; koma zinthu zosaoneka n'zamuyaya" (2 Akorinto 4:4-18).

Ngati tikonda Mulungu ndi moyo, tipumula. "Ndipo kwa inu amene mukuvutika pumulani [mwa Yesu] nafe" (2 Atesalonika 1:7). Bwerani kwa Ambuye tsopano lino ndi kupulumutsidwa komanso kupumula pakunena pemphero ili:

AMBUYE wanga komanso MULUNGU wanga, ndichitireni chifundo ndine munthu wochimwa.⁵ Ndikukhulupirira kuti YESU KHRISTU ndi MWANA wa MULUNGU wamoyo.⁶ Ndimakhulupiriranso kuti IYE anafera pamtanda ndipo anakhetsa mwazi WAKE wamtengo wapatali ndi cholinga choti machimo anga onse akhululukidwe.⁷ Ndikukhulupiriranso kuti MULUNGU anaukitsa YESU kwa akufa pogwiritsa ntchito mpham-

vu ya MZIMU WOYERA,⁸ ndiponso kuti IYE anakhala kudzanja lamanja la MULUNGU ndipo panopa akumva pemphero langa lolapali.⁹ Ndikutsegula zitseko za mtima wanga, ndipo ndikukuyitanani kuti mulowe mumtima mwanga, inu AMBUYE YESU.¹⁰ Tsukani machimo anga ambirimbiri achoke onse mu mwazi wamtengo wapatali umene INU munakhetsa m'malo mwanga pamtanda wa ku Kavari.¹¹ Ndikudziwa kuti mundimvera pemphero langali AMBUYE YESU; INU mukhululukira machimo anga ndi kupulumutsa moyo wanga. Ndikudziwa izi chifukwa MAWU ANU, Baibulo, limanena zimenezi.¹² MAWU ANU amati INUYO simudzakana kumvetsera pemphero la munthu aliyense, ndipo ine ndili m'gulu la anthu amenewo.¹³ Choncho, ndikudziwa kuti INUYO mukundimvetsera pamene ndikupemphera ndipo ndikudziwanso kuti INUYO mundiyankha komanso mundipulumutsa.¹⁴ Ndipo ndikukuthokozani AMBUYE YESU, chifukwa chopulumutsa moyo wanga, ndipo ndisonyeza kuyamikira mwa kuchita zinthu zimene INUYO munalamula komanso kupewa kuchita uchimo.¹⁵

Pambuyo pa chipulumutso, YESU ananena kuti munthu ayenera kubatizidwa pomizidwa thupi lonse m'madzi, m'dzina la ATATE, ndi la MWANA, ndi la MZIMU WOYERA.¹⁶ Muziphunzira mwakhama Baibulo la *Buku Lopatulika Ndilo Mau a Mulungu*, [King James Version] ndipo muzichita zimene Baibulolo limanena.¹⁷

AMBUYE akufuna kuti inuyo muziwuza ena za chipulumutso chanu. Mungathe kukhala wofalitsa uthenga wabwino wa Mbusa Tony Alamo. Tizikutumizirani mabuku mwaulare. Imbani foni kapena tumizani imelo kwa ife kuti mudziwe zambiri. Tikukupemphani kuti muwuzeko ena uthengawu.

Ngati mukufuna kuti dziko lipulumutsidwe monga m'mene YESU akulamulira, mukufunika kupereka chakhumi kwa MULUNGU. MULUNGU anati, "Kodi munthu angabere MULUNGU? Inde, mwandibera kale. Koma akuti, Ife tikumubera bwanji MULUNGU? Mu chakhumi ndi mu zopereka. Anthuwo ndi otembereredwa chifukwa akundibera, ngakhale mtundu wonsewu [dziko lonse lapansi]. Bweretsani nonse chakhumi ['chakhumi' ndi gawo limodzi la magawo khumi (10%) ya malipiro anu] m'nkhoke zanga n'cholinga choti pakhale nyama [chakudya cha Uzimu] mu nyumba YANGA [anthu opulumutsidwa] kuti mundiyese, akutero AMBUYE wa MAKAMU, kuti muone ngati sindidzakutsegulirani mazenera a Kumwamba ndi kukukhuthulirani madalitso amene mudzasowa malo owalandirira." Ndipo ndidzadzudzula anthu okudyerani masuku pamutu ndipo sadzawononga zipatso za nthaka yanu; ngakhale mphesa wanu sudzalephera kubala zipatso pa nyengo yake m'minda yanu, watero AMBUYE wa MAKAMU. Ndipo mitundu yonse idzakutchani odala: chifukwa dziko lanu lidzakhala labwino, watero AMBUYE wa MAKAMU" (Malaki 3:8-12).

5 Sal. 51:5, Aro. 3:10-12, 23 6 Mat. 26:63-64, 27:54, Luka 1:30-33, Yoh. 9:35-37, Aro. 1:3-4 7 Mac. 4:12, 20:28, Aro. 3:25, 1 Yoh. 1:7, Chiv. 5:9 8 Sal. 16:9-10, Mat. 28:5-7, Marko 16:9, 12, 14, Yoh. 2:19, 21, 10:17-18, 11:25, Mac. 2:24, 3:15, Aro. 8:11, 1 Akor. 15:3-7 9 Luka 22:69, Mac. 2:25-36, Aheb. 10:12-13 10 1 Akor. 3:16, Chiv. 3:20 11 Aef. 2:13-22, Aheb. 9:22, 13:12, 20-21, 1 Yoh. 1:7, Chiv. 1:5, 7:14 12 Mat. 26:28, Mac. 2:21, 4:12, Aef. 1:7, Akol. 1:14 13 Mat. 21:22, Yoh. 6:35, 37-40, Aro. 10:13 14 Aheb. 11:6 15 Yoh. 5:14, 8:11, Aro. 6:4, 1 Akor. 15:10, Chiv. 7:14, 22:14 16 Mat. 28:18-20, Yoh. 3:5, Mac. 2:38, 19:3-5 17 Deut. 4:29, 13:4, 26:16, Yos. 1:8, 22:5, 2 Tim. 2:15, 3:14-17, Yak. 1:22-25, Chiv. 3:18

Ngati mukufuna kudziwa zambiri kapena ngati mukufuna mabuku kapenanso nkhani zina zimene zimakusangalatsani, tiimbireni foni kapena tilembeni.

Tony Alamo, World Pastor, Tony Alamo Christian Ministries Worldwide • P.O. Box 2948, Hollywood, CA 90078

Twenty-four hour prayer and information line: +1 (661) 252-5686 • Fax +1 (661) 252-4362

www.alamoministries.com • info@alamoministries.com

Tony Alamo Christian Ministries Worldwide imalandira anthu onse ndipo imapereka zinthu zofunika kwa onse amene ali ku U.S. amene akufunitsitsadi kuti ayambe kutumikira AMBUYE ndi mtima wawo wonse moyo wawo wonse ndi mphamvu zawo zonse

Mapemphero amachitika usiku uli wonse nthawi ya 8 Koloko usiku ndi Lamulungu nthawi ya 3 Koloko madzulo ndiponso

8 Koloko usiku ku Tchalitchi cha kudera la Los Angeles: 13136 Sierra Hwy., Santa Clarita, CA 91390, +1 (661) 251-9424

Magalimoto a ulere opita ndi kuchokera ku mapemphero amaperekedwa pa kona ya Hollywood Blvd. ndi Highland Ave.,

Hollywood, CA tsiku lili lonse nthawi ya 6:30 madzulo, Lamulungu lili lonse nthawi ya 1:30 madzulo ndi 6:30 usiku.

Mapemphero amachitika mu Mzinda wa New York Lachiwiri lili lonse nthawi ya 8 Koloko usiku ndi madera ena usiku okhaokha. Chonde

imbani foni kuti mumve zambiri: +1 (908) 937-5723. ZAKUDYA ZIMAGAWIDWA PA MAPETO PA MAPEMPHERO ALI WONSE

Funsani buku la M'busa Alamo, lakuti Mesiya, losonyeza KHRISTU kuyambira ku Chipangano Chakale mu maulosi oposa 333.

Khalani wogwira ntchito yokolola miyoyo ya anthu pakukhala ogawira mabuku a M'busa Alamo

Mabuku ndi zinthu zonse zomvetsera n'zaulere, ndipo simulipira ndalama yotumizira

Ngati wina akukuuzani kuti mupereke ndalama pa zinthu zimenezi, chonde imbani pa (661) 252-5686.

M'BUKU ILI MULI CHIKONZERO CHENICHENI CHA CHIPULUMUTSO (Machitidwe 4:12).

MUSALITAYE, PATSANI ENA KUTI AWERENGE.

Anthu amene muli m'mayiko ena, tikukulimbikitsani kuti mumasulire n'chinenero chanu mabukuwa. Ngati

mukusindikizanso bukuli, musaiwale kuika mawu ali m'munsiwa omwe ndi okhudzana ndi zamalamulo:

© Copyright October 2010, 2015 All rights reserved World Pastor Tony Alamo © Registered October 2010, 2015

CHICHEWA/NYANJA—VOLUME 11100—RESTING IN THE TIME OF TROUBLE